

A White kuonetsa ina mwa mitengo yomwe yaonongeka paofesi ya sikimu ya Muona

# Alonjeza kubwezeretsa mitengo yoposa 200 ku Muona

WOLEMBA:
**MARTIN GELA**

Akuluakulu oyendetsa sikimu ya Muona kwa T/A Mlolo m'boma la Nsanje adandaula ndi momwe namondwe wa Freddy wasakazira mitengo kuzungulira sikimuyo.

Wapampando wasikimuyo a Alex Paraffin anati mitengo yokwanira 48 ikuluikulu yagwetsedwa ndi namondwe wa Freddy zomwe zikupereka chiopsezo choti ofesi yawo ikhoza kukanthidwa ndi mphepo ya mkutho yomwe nthawi zambiri imakonda kuyalula madenga.

Iwo adati: "Tagwirizana kuti tipeze mbande za mitengo200 kuti tibzale mozungulira ofesi yathu komanso tikufuna kubwezeretsa mitengo ina m'mbali mwa mtsinje wa Muona-Thangadzi omwe panopa wasintha kolowera."



CHITHUNZI: MARTIN GELA

Moyo: Alimi ayenera kupeza mitengo

A Paraffin adati izi zachititsa kuti mudzi onse wa a Mfumu a Chipondeni usamuke popeza ngakhale a Agricultural Commercialization Project (Agcom) kudzera m'chiringanizo chawo cha Last Mile adatimangira kuti madzi asatizunze, dyke m'Chingerezi, koma lidapita ndi madzi. Iwo adaonjeza kuti anthu akukhalira mphanthi popeza chipatala cha Muona, sukulu ya pulaimale ya Muona, kachisi wa mpingo wa Seventh Day Adventist omwe ndi eni a sukuluyo ndi bwalo la milandu zakwiririka.

Pogwirizana ndi a Paraffin, a Elias White a m'mudzi wa Khavala adati ngakhale akonza mapulani wofuna kubwezeretsa mitengoyi iwo ngati alimi alibe mbewu ndi mitengoyo. Choncho anapempha a kufuna kwabwino kuti abwere awathandize ndi mitengo.

A White anati pakufunika kuti boma ndi adindo alingalire mozama kuti awapatse tchinga lomangira simenti ngati lomwe anamanga pamtsinje wa Nafafa lomwe likutetezera anthuokhala m'midzi ya Khavala, Nalisoni ndi Chapinga popeza poyamba anthuwa amazunzika ndi madzi.

Mkulu woona zaulimi wa mthirira m'boma la Nsanje a Jacob Henry Moyo anati ayesetsa kuti alimiwa apeze mitengo yoti abwezeretse yomwe yaonongeka ndi namondwe wa Freddy.

Iwo adati: "Tikuthokoza a Shire Valley Transformation Programme (SVTP) omwe akuthandizira kuti tione zomwe zaonongeka m'masikimu athu kuphatikizirapo kuona zachilengedwe zomwe tikuyenera kuti tibwezeretse monga mitengo ndi zinthu zosiyanasiyana." ■

## BWALO LA ULIMI



WOLEMBA: ANDREW SAUKANI

# Pulojekiti ya Trade

Zikamativuta pa chitukuko cha ulimi kumangokhala kusamvetsetsa kuti ndi chani tikusowa. Maunduna a za malimidwe, chitukuko cha madzi ndi za chilengedwe kumapita thandizo lochuluka kudzera m'mapulojekiti osiyanasiyana.

Pulojekiti imabwera ngati ngongole zimene boma limatenga kuti ithandizire kugwirira ntchito zina ndi zina zotukula ulimi komanso miyoyo ya anthu. Ngakhale zimakhala ngongole koma mbali ina imakhala mphatso chabe kuchokera ku maiko othandiza pamene ndalama zina zimakhala msonkhasonkha wa boma.

M'zaka 5 zikudzazi, kudzera ku unduna wa maboma aang'ono kukhala kukugwiridwa ntchito yosintha ndi kutukula ulimi ngati bizinesi yotchedwa Transforming Agriculture through Diversification and Entrepreneurship (Trade). Cholinga cha polojekitiyi ndi kutukula miyoyo ya alimi m'madera a ku mudzi poonetsetsa kuti akulima mbewu kapena ziweto zimene akupeza nazo phindu akapititsa kumisika.

Pulojekitiyiyatsindika pa mbewu ndi ziweto zimene zili ndi kuthekera kokonzedwa bwino kuti zikathe kuonjezera phindu kumsika. Pulojekiti ilimbikitsa ubale pakati pa alimi ndi ogula kuti katundu asamangopita mwachinunu mosakonzedwa bwino kumene kuti kutaya phindu.

Alimi alimbikitsidwa kukhala m'magulu a makoperativu. Kuti izi zitheke, alimi akuphunzitsidwa luso ndi ukadaulo osiyanasiyana malingana ndi mbewu kapena ziweto zimene ali nazo. Pakhalanso maphunziro kathithi a kachitidwe ka bizinesi mwaphindu komanso ulimi ogwirizana ndi kusintha kwa nyengo.

Ntchito zimene zigiwiridwe m'pulojekiti ya Trade sizikusiyana kwambiri ndi chilinganizo cha Rural Livelihoods and Economic Enhancement Programme chimene chinali ndi zofooka zina zimene zikonzedwe ulendo uno pofuna kukwaniritsa kutukula miyoyo wa anthu kudzera ku ulimi m'madera a ku mudzi.

Pulojekiti ya Trade ifikira alimi m'maboma 11 kumene boma lililonse lilimbikitsa ulimi wa mbewu kapena chiweto chimodzi chimene chikuoneka kuti chitha kuthandizira pa zolinga za pulojekitiyi.

Maboma a Chitipa, Karonga ndi Rumphi, pulojekiti ilimbikitsa ulimi wa ng'ombe za nyama, ku Nkhata Bay akhala akulimbikitsa ulimi wa njuchi. M'maboma a Kasungu, Mchinji, Ntchisi ndi Lilongwe, pulojekiti ilimbikitsa ulimi wa soya ndi mtedza pamene ku Dedza ikhazikika pa ulimi wa soya ndi mbatatesi ya kachewere.

Kuchigawo cha kumwera, pulojekitiyi ili m'maboma Thyolo ndi Blantyre kumene ilimbikitse ulimi wa ng'ombe za mkaka. Pali chiyembekezo kuti pakutha pa zaka 5 anthu okwana 1.3 miliyoni apindula ndi ntchitoyi pamene alimi okwana 127 000 ndi amene akhudzidwe kwambiri malingana ndi magawo amene akuchita.

Anthu okwana 173 000 akhudzidwa m'njira zina ndi zina maka pantchito zomanga misewu ndi zina. Pulojekiti ya Trade ikulandira thandizo kuchokera ku bungwe la IFAD ngati ngongole yokwana $51.1 miliyoni, $18.9 miliyoni ngati mphatso pamene $15.3 miliyoni ichokera ku boma la Malawi. ■

*Mafunso: saukaniandrew@gmail.com*